Mmene Zochita za Angelo Komanso Ziwanda Zimakhudzira Moyo Wathu (Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 10 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI ANGELO NDI NDANI?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena amanena zotani?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Angelo ali ndi matupi auzimu ndipo ndi amphamvu, anzeru komanso amatha kusangalala kapena kukhumudwa.
(Werengani mutu 10 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1 mpaka 5.)

Werengani Yobu 38:4-7, Salimo 103:20 ndi Luka 15:10.
Kodi malembawa akusonyeza bwanji kuti angelo ali ndi mphamvu, nzeru komanso amatha kusangalala?

Werengani Danieli 6:22 ndi Machitidwe 12:6-11.
Kodi angelo okhulupirika anathandiza bwanji anthu a Mulungu akale?

Angelo amasangalala munthu wochimwa akabwerera kwa Yehova.—Luka 15:10

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Angelo ena ndi oipa.

(Werengani mutu 10 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 6 mpaka 8.)

Werengani Chivumbulutso 12:9.

Kodi lembali likusonyeza kuti Satana Mdyerekezi ndi mngelo yekhayo amene anagalukira Mulungu?

Werengani Genesis 6:2.

Kodi ziwanda zinagalukira bwanji Mulungu?

Werengani Salimo 34:7.

Kodi mumamva bwanji mukaganizira kuti Yehova amagwiritsa ntchito angelo okhulupirika kuti azitiiteteza kwa angelo oipa amene akufuna kusokoneza ubwenzi wathu ndi iye?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Si zoona kuti kuli angelo.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri akhoza kuganiza choncho. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Ine sindinaonepo angelo, ndiye ndimaona kuti sangandichitire chilichonse.

MUNGANENE KUTI…

N’zoona kuti angelo saonekera kwa anthu ngati mmene ankachitira kale. Koma ndimakhulupirira kuti zochita zawo *zimakhudza* moyo wathu chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania